# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA ZANYENGO

### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA MULANJE M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


- Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi El Nino wokula mphamvu. El Nino ndi kutentha kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific.
- Boma la Mulanje likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo **wokhazikika kapena kuposela apo**. Ngakhale izi zili choncho, pali chiyembekezo cha mvula ya mlingo otsikilapo mu mwezi wa November 2024.

## October 2024





Mwezi wa October ukuyembekezeleka kukhala ndi mvula ya mulingo okhadzikika wapakati pa 10-70mm madera ambiri Mvula yoyambilira itha kudzabwera ndi mphepo yamkuntho komanso ziphaliwali.

## November 2024





Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 140mm ikuyembekezeleka mu mwezi wa November omwe udzakhale mlingo okhadzikika. Chiyembekezo cha mphepo ya mkuntho komanso ziphaliwali ndichokwera mweziwu.
Mvula yodzalira ikuyembekezereka madera ena kuyambila sabata yachitatu ya mwezi wa November m'bomali.

## December 2024





Madera ambiri makamaka a chigawo cha kumawa ndi pakati kwa Mulanje akuyembekezereka kulandira mvula ya mulingo ochulukirapo kusiyana ndi madera ena m'bomali. Madera ozungulira Phiri la Mulanje, Sc Laston, Njema ndi TA Mabuka ali ndikuthekera kolandira mvula ya mulingo wa pakati p 250 ndi 350mm Madera a ku mpoto kwa Muanje monga SC Juma ndi TA Nkanda akuyembekezereka kulandira mvula ya pakati pa 160mm ndi 200mm

## January 2025





Mvula yochulukilapo ikuyembekezeleka mu mwezi wa January. Mvula yochuluka ya mlingo wapakati pa 300mm ndi 490mm ikuyembekezeleka mmadera ambiri monga TA Mabuka, Mulanje Boma ndi Mulanje Mountain Reserve
Madera ozngulira TA Nthiramanja, Chikumbu, Nkanda ndi SC Juma akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wapakati pa 260-300mm

## February 2025




Mu mwezi wa February, pali kuthekela kolandila mvula ya mlingo okhazikika kapena oposera apo madera ambiri m'bomali. Mvulayi ikuyembekezeleka kukhala ya mlingo wa pakati pa 160mm ndi 200mm. Mvula yochulukilapo ikuyembekezeleka mmadera ozungulira Mulanje Boma and SC Laston Njema pa mlingo wa pakati pa 230 ndi 350mm.
Pali kuthekera kokhala ndi masiku a ng'amba osaposa sabata imodzi mweziwu.


## March 2025




Mwezi wa march madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula yochuluka .
Mvula ya mlingo wa pakati pa 250-360mm ikuyembekezereka kugwa madera ena monga SC Laston Njema, TA Mabuka ndi Mulanje Boma.

Madera a kumpoto kwa bomali monga TA Nkanda ndi SC Juma akuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 170-230mm


## April 2025




Nyengo ya dzinja idzakhala ikupita kumapeto, madera ochuluka a m'bomali pomafika sabata lachitatu, ndipo madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula yochulukirapo kuposa mlingo okhadzikika wa pakati pa 70-300mm mu mweziwu

*Boma la Mulanje likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposela apo. **Mvula yodzalira** ikuyembekezereka pakati **pa sabata yachitatu ya mwezi wa November ndi sabata yoyamba la mwezi wa December 2024**.Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka **kudzatha kuyambira sabata yachitatu ya mwezi wa April 2025.** Nyengo ya dzinjayi ikuyembekezeka **kokhala yotalika masiku a pakati pa 130 ndi 150.** Pali kuthekera kokhala ndi masiku a ng'amba osaposa sabata imodzi mwezi wa February 2025*

| MIMOSA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 19.5 | 69.2 | 28.8 |
| NOV | 98.4 | 138.7 | 122.1 |
| DEC | 188.7 | 329.7 | 284.2 |
| JAN | 223.7 | 401.1 | 412.2 |
| FEB | 214.1 | 271.1 | 298.8 |
| MAR | 166.8 | 291.2 | 294.4 |
| APR | 65.0 | 160.8 | 122.1 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**


The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw


Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: